ttb_Nya_0833_script

1 Atesalonika : 5:1-11

Mutu : Chiyembekezo chakudzakwa Kristu chitilimbikitse kutumikira Mulungu

Ndipereka moni wa Kumwamba kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyamba ndi mau apa Yakobo 4:6, amene akuti "Mulungu akanizaodzikuza, koma apatsa chisomo odzichepetsa." Tsono mupologalamu yatha tinali kusanthula 1 Atesalonika 4:13-18, momwe timakambirana za ziphunzitso zina zokhudzamkwaturo. Ndipo lero pa 1 Atesalonika 5:1-11, tikambirana kuti chiyembekezo chakudzakwa Kristu chitifulumize kutumikira Mulungu.

Chapter 5 chimawona zimene akhristuayenera kuchita chifukwa chakubwerakwa Ambuye. Mukumbukira kuti mu chapter1,tidaphunzira za maganizo woyenera kukhala nawo pa zakubwera kwa Ambuye. Kubweranso kwa Ambuye ndi nkhani yopatsa chiyembekezo ndipo chiyembekezo chimenechochimatipangitsa kuchitapo kanthu.

Okhulupirira mwa Ambuye akhale maso kuyang'anira kubwera kwa Ambuye chifukwa tsiku limeneli lidzatipulumutsa ku chizunzo chimene chidzafike kutsatira usiku wa Tsiku la Ambuye. Tsiku la Ambuye likuyamba ndi usiku chifukwa ndi momwe nthawi ya Mulungu imayambira.Mulungu amayamba ndi usiku koma amapita ku kuwala. Chomwecho nthawi ya chizunzoidzathera mu nthawi ya ulamuliro waulemelero wa Ambuye pamene Dzuwa la Chiyerolidzawalapamapiko a Ambuye.

1. Koma za nthawizo ndi nyengozo, abale sikufunika kuti ndikulembereni.

Pamene Paulo akukamba za nthawizo ndi nyengozo, ndiye kuti akunena zakubwera kwa Yesu Khristu. Pa Tsiku la Ambuye ana a Israeli ndi a Helene onse adzapulumutsidwa. Mpingo sukufunikanso chiphunzitso china chokhudza nthawi ndi nyengo chifukwa Paulo adafotokoza kale zazimenezi.Pachifukwa chimenechi Paulo sakufuna kulembanso zinthu zotiadalemba kale.Paulo anali wokhutitsidwa kuti adafotokozakokwanirazazimenezi ndipo kunali koyenera kuti azikumbukira.Ndiye tikunenetsa kuti Paulo anali ataphunzitsa kale

zakubweransokwa Ambuye.Onani pa 1 Atesaalonika 1:10 tipeza mau akuti, “Ndikulindirira Mwana wake achokere Kumwamba, amene adamuukitsa kwa akufa, ndiye Yesu wotipulumutsa ife ku mkwiyo ulimkudza.”

Wokondedwa anzanga apaulendo, Ambuye Yesuadzabwera ngati mbala, koma okhulupirirasadzadzidzimuka pa Tsiku la Ambuye chifukwa akuyembekeza Tsiku limeneli.Amene adzadzidzimuke ndi anthu akunja chifukwa amangokhalamopanda chiyembekezo.M’Chipangano Chakale sitiwerenga za mkwatulo koma timamva za Tsiku la Ambuye.Pa tsiku la Mkwatulo chisomo chimene timayendamondikukhalamo lero chidzatha.Patsikulokudzayambikachizunzo, chiyambi cha Tsiku la Ambuye. Anthu akhoza kukhazikika mu mphamvu ya ulamuliro wa dziko lino ndi chuma koma ana a Mulungu ayenera kukhala tcherukuyang’anira tsiku la kubwera kwa Ambuye.

2. Pakuti inu nokha mudziwa bwino kuti tsiku la Ambuye lidzadza monga mbala usiku.

Paulo akunenetsa kuti Ambuye Yesu adzabwera ngati mbala, panthawi yosadziwika, koma sadzafika ku mpingo wake modzidzimutsa chifukwa Mpingo ukuyang'anira kubwera kwa Ambuye. Kutanthauza kuti Yesu adzafika ngati mbalakwa iwo amene sadziwa zakubwera kwake kapena amene sakhulupilira zakubwera kwake. Kwa osakhulupirira Yesu adzafika ngati mbala chifukwa pa nthawiyookhulupirira adzakhala atakwatulidwa.

Pakuti inu nokha mudziwa bwino– kutanthauza kuti anali atawaphunzitsa bwino za zimenezi. Paulo amatsimikiza mtima za zimene adaphunzitsa ku mipingoyomweadayitumikira kotero kuti amadziwa mosakayikira zimene mipingoyoimadziwa.

Tsono Tsiku la Ambuye lidzadza monga mbala usiku.Kutanthauza kuti tsikulilidzafika mwadzidzidzi, mosayembekezeka.Tsikulilidzafikamopandakulengeza tsiku lake ndi nthawi yake.Ambuye adzafikamosayembekezakudzaweruza.Pachifukwa ichi palibe munthu angalosere tsiku limene adzabwere Ambuye.Kulosera tsiku kapena chaka chimene adzabwere Ambuye ndikudzinyenga chabe

komanso kunyenga anthu. Kodi ngati kuli kotheka kulosera za tsikulo ndiye adalifanizira bwanji ndi kubwera kwambala? Tiyenitisanyengedwe ndi aphunzitsi onyenga amene amalankhula ngati akudziwa chaka ndi tsiku lobwera Ambuye.

3. Pamenepo angonena, Mtendere ndi mosatekeseka, pamenepo chiwonongekochobukapochidzawagweraiwo, monga zowawa za mkazi wa pakati; ndipo sadzapulumuka konse.

Pano tiyambe ndi mau akuti Paulo m'ndime ziwiri zoyambilira amalankhula za okhulupirira. Koma apa pali kusintha. Iye, akunena za anthu osakhulupirira, popeza panthawi imeneyi okhulupiriraonse adzakhala atakwatulidwa kale.

Tibwerezenso kunena kuti Tsiku la Ambuye lidzayambandiChizunzo chimene chikathere mu ulamuliro waulemelero wa Yesu Khristu. Tamvani Yesaya 13:9-10, "Taonani Tsiku la Yehova lidza, lankhanza, ndi mkwiyo ndi kukalipirakwaukali; kupasula dziko, ndi kudzaonongamoakuchimwapsiti. Chifukwa nyenyezi za Kumwamba ndi makamu awo sizidzawala; dzuwa

lidzadam'kuturuka kwake, ndipo mwezisudzawonetsa kuwala kwake."Mneneri Yoweli 1:15; 2:2, akunenetsa kuti tsiku limeneli silidzakhala la masewera; "Kalanga ine, tsikuli! Pakuti layandikiratsiku la Yehova, lidzafika ngati chiwonongekochochokerakwa Wamphamvuyonse ...Tsiku la m'dima, la mdima wandiweyani, tsiku la mitambo,mitamboyochindikira ngati m'mbandakuchamoyalikapamapiri; mtundu waukulu ndi wamphamvu, panalibe wotere utapita uwu, kufikira zaka a mibadwo yambiri."

Ichi ndiye chithunzi chimene timawona m'Chipangano Chakale. Tsiku la Ambuye lidzayamba ndi nthawi ya chizunzo ndipo idzapitirira kufikira nthawi ya ulamuliro waYesu Khristu. Chithunzi ichi, ndiwo mutu waukulu m'Chipangano Chakale.

Koma nkhani ya mkwatulo imene tinasanthulam'chaputala 4 sitiyipezamwachindunji m'Chipangano Chakale.Komabe timapeza nkhani zina zimene zimatipatsachithunzithunzi cha zimene zidzachitike.Mwachitsanzo nkhani ya Enoki ndi ndi Eliya.Awiri

onsewa sadafe, adatengedwa amoyo kupita Kumwamba. Koma sitiwerengazokambazakutengedwakwa anthu okhulupirira ndi Yesu m'Chipangano Chakale ayi. Tsono Yesu mwini ndiye ameneadafotokoza nkhaniyi koyamba mwabvumbulutsola chowonadi chake pa Yohane 14:2-3 pamene adanena kuti; "M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri.Ngati sikudalikutero, ndikadakuwuzani inu; pakuti ndipitakukakukonzerani inu malo.Ndipo ngati ndipitakukakonzera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso."

Tere Paulo adalembamotsatila zimene Yesu adaphunzitsaophunzira ake.Koma zimene tikuwerenga mu 1 Atesalonika 5 ndi nkhani yakuti imadziwika kuyambira Chipangano Chakale.Zidzakhala zinthu zochitika mwadzidzidzi ku dziko lapansi.Palibe amene adzakhaleakuyembekezera kuti zochitikazi.Lonjezo la mtendere ndi chitetezo ndi 'bodza lalikulu' limene tidzawone mu 2 Atesalonika 2. Yesu adachenjeza za zinthu izi pamene adanena kuti:"Chenjerani kuti asadzakunamizeni." Dziko lapansi likuganiza kuti likulowa m'nyengo ya mtendere koma lidzadzidzimukalitalowam'chizunzo

chachikulu.Tsiku limeneli lidzafika mwadzidzidzi ngati mbala usiku.

4. Koma inu, abale, simuli mumdima, kuti tsikulolikakugwereni monga mbala.
5. Pakuti inu nonse muli ana a kuunika, ndi ana a usana; sitiri a usiku, kapena amdima.

Pa tsiku la mkwatulokudzakhlakuthakwa nyengo ina komansochiyambi cha nyengo ina. Mwanjira ina kunena kuti mkwatulo wa mpingo ukadzachitika zinthu ziwiri zidzachitika:

I. Nyengo ya chisomo imene tikukhalamo lero idzathakutanthanthauza kuti Uthenga Wabwino sudzalalikidwanso ndipo sikudzakhalansokothekakuti munthu wina akhoza kuyitanira pa dzina la Ambuye. Kunena kuti palibe munthu amene adzapeza chikhululukiro cha machimo panthawi imeneyi.
II. Ndiye pamene nthawi iyi, idzatha chidzakhala chiyambi cha Tsiku la Ambuye. Chinzunzo chachikulu chidzayambika ndipo mpingo udzachoka padziko lapansi.

Ndiye ndichifukwa chake Paulo akunena kuti, “Koma inu, abale, simuli mumdima, kuti tsikulolikakugwereni monga mbala.” Kutanthauza kuti kwa abale okhulupiriratsikulisilidzafika ngati mbala imene imafikamum’dima chifukwa adzakhala atakwatulidwa. Monga tidawonam’chaputa 4, Ambuye mwini wake adzatsika ndi mfuwu waukulu ndikutenga mpingo wake kuchoka padziko lapansi.

Ndiye akupitiliza kunena kuti, “Pakuti inu nonse muli ana a kuunika, ndi ana a usana.”Kutanthauza kuti abale onse okhulupirira si ana anyengo ya m’dima, nyengoyachizunzo chimene chiri nkudza.Tikutsindika kuti abale okhulupirira onse khalani ndi kulimbika mtima chifukwa ndinu ana a nyengo ya chisomo imene tikukhalamo lero.

Wokondedwa anzanga apaulendo, uku ndiko kusiyana pakati pa okhulupirira ndi osakhulupirira ndi zimene zidzatsatira aliyense monga mwa mbali imene aliri. Mau a Mulungu amatiwonetseratumwachimvekere kusiyana kwambali iliyonse, ya okhulupirira ndi ya osakhulupirira. Pachifukwa ichi, khalani ndi

chidwi kuwerenga ndi kuphunzira Mau a Mulungu kuti musanyengedwe.

Tsono Tsiku la Ambuye likadzafika, tidzakhala ndi Ambuye. Pankhani iyi, Mau a Mulungu sanatisiyemum'dima pakuti sindife ana a m'dima. Choncho tsiku limenelo kwa ana kuunika, ana a usana silidzafika ngati mbala. Ambuye sadzafika kudzatenga mpingo wake ngatimbalapopeza okhulupirira"Akulindirira chiyembekezo chodala, ndi maonekedwe a ulemerero wa Mulungu wamkulu ndi Mpulumutsi wathu Khristu Yesu" (Tito 2:13). Tsono tikunenetsa kuti kubwera kwambalasichiyembekezo chimene munthu ungachilindire ngati madalitso ayi. Akhristuakulindirira kubwera kwa Ambuye mwa chiyembekezo chodala. Choncho Paulo akulimbikitsa akhristu motere:

6. Chifukwa chake tsono tisagone monga achitira enawo, komatu tidikire, ndipo tisaledzere.

Monga tawonakale kutimkwatulo, ndi chiyembekezo chathu chodala, ndipo wayandikira.Pachifukwa ichi tiyenera kukhala tcheru, osakhala ngati anthu osakhulupirira ayi.Tiyeni tikhale

tcheru, tiyimepamalonjezano a Mulungu.Akhristu ena agonatulondikukhalamotayilira.Ambiri akhazikika pa zinthu zadziko, kotero kuti akungokhalamosayang'anira ngati sakumva kuti nthawi yatsala pang'ono.Timayimba nyimbo ija yakuti 'Kwathu SipadzikoNdingopitilira' koma ena akuyimbaatakhazikika pansi pompano ngati opanda chiyembekezo.Kodi inumukukhalamwatcheru kapena mwagonatulo? Nkhani ikuti Ambuye adzatsika mwini yekha kudzatenga mpingo wake ndipo tiyenera kukhala tcheruosagona ngati momwe akuchitira anthu opanda chiyembekezo. Tikhale tikudikiramwatcheru, osati ngati oledzera.

Tsono pankhani yakuledzera, tikhoza kuona kuledzera ndi zakumwazoledzeretsa kapena mankhwalaozunguza bongo.Koma taonani lero anthu ambiri masiku ano ndi oledzera chifukwa cha mphamvu yaulamuliro, udindo, chuma ndi zinthu zina zadziko lapansi.Ndiye Paulo akunenetsa kuti ana a Mulungu ayenera kukhala osaledzerapodikira kubwera kwa Ambuye popeza kuti nthawi yakubwera kwa Ambuye yayandikira. Sitingatchule tsiku lake ndi nthawi yake yeniyeni, koma Mau a Mulungu akutiwuza

mosakayika kuti tsopano nthawi ili pafupi. Tere ndichifukwa chake Paulo pa Aroma 13:11, akunena kuti, “Ndipo kuti, podziwa inu nyengo, kuti tsopano ndiyo nthawi yabwino yakuwuka kutulo; pakuti tsopano chipulumutso chathu chiri pafupi koposa pamene tidayamba kukhulupirira.”

7. Pakuti iwoakugona, agona usiku; ndi iwo akuledzera aledzera usiku.
8. Koma ife popeza tiri a usana tisaledzere, titabvalachapachifuwa cha chikhulupiriro ndi chikondi, ndi chisotichiri chiyembekezo cha chipulumutso.

Paulo akubwerezansokutichenjeza kuti tisakhale ngati oledzera.Tiyenera kuzindikira kuti tili pa nyengo yofunika kukhala tcheru.Woledzera sakhala munthu watcheru, sagwira ntchito molongosoka.Tiri ndi udindo wofunika kukhala atcheru.Ndiye tiyenera kuchita izi, titabvalachapachifuwa cha chikhulupiriro ndi chikondi, ndi chisoti chimene ndi chiyembekezo cha chipulumutso.Kutanthauza kuti inu ndi ine, tiri ndi udindo ngati wamsirikali. Titabvalachapachifuwa cha chikhulupiriro ndi chikondi kutchinga pa mtima, chimene ndi chiwalo chofunika

kwambiri pa moyo wa munthu. Tsono chisoti ndi chiyembekezo cha chipulumutso.Mwachisoni kuti masiku ano wokhulupirira ambiri amayenda osabvalazisoti.Kutsimikiza kuti wokhulupirira akuyendamopanda chiyembekezo.

Tsono Paulo akubwereza mau a Chikhulupiriro, chikondi ndi chiyembekezo.Aka ndikachitatu tsopano mkalata iyi kuwerenga za mau amenewa.Monga adalembapoyamba paja za chikondi chochitachita, ntchito zachikhulupirirondi chipilirochachiyembekezo.Kutanthauza kuti chipulumutso chimachokera ku chikhulupiriro, ndipo chipulumutso chochokera ku chikhulupiriro chimabala ntchito zachikhulupiriro.

Tsono chikhulupiriro chimayang'ana m'mbuyo kuchokera pa tsiku limene mkhristuadapulumutsidwaatakhulupirira Yesu Khristu.Komanso chikhulupiriro chimawoneka tsiku ndi tsiku mwachikondi chimene wokhulupirira amawonetserakwa anthu ena. Chiyembekezo chachipulumutsochimene ndi chiyembekezo chodalandi chimene tikudikira.Ichi, chiyembekezo chodala chimene chidzawoneka Ambuye akadzabwerakudzatenga okhulupirira.1 Yohane 3:2, akunena kuti, "Wokondedwa, tsopano tiri ana a

Mulungu, ndipo sichidawoneke chimene tidzakhala.Tidziwa kuti, pa kuwoneka Iye, tidzakhalawofanana ndi Iye, pakuti tidzamuwona Iye monga ali.”Kunena kuti Mulungu akadatikonzabe.Ndipo simuyenera kutaya mtima ndi anzanu okhulupirira kapena ndi inu nokha ayi.Khalani ndi chipiriro cha chiyembekezo.Ambuye adzamaliza ntchito imene idayiyamba mwa inu ndi mwa okhulupirira onse.Ichi, ndichimene Paulo anali kunena pa Afilipi 1:6, pamene anati, “Iye amene adayamba mwa inu ntchito yabwino, adzayitsiriza kufikira tsiku la Yesu Khristu.”

9. Pakuti Mulungu sadatiyikaifetilawe mkwiyo, komatu kuti tilandire chipulumutso mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.

Paulo pano akuti Ambuye adamva zowawa m’malo mwathu kotero kuti adatichotsera zowawa za nthawi ya chizunzo chachikulu.Mwachisomo cha Mulungu adatipulutsa ndipo chifukwa cha chisomo chomwecho, adzatipulutsa nthawi ya chizunzo. Ambuye akadzabwera kudzatenga mpingo wake adzatitenga mwachisomo cha Mulungu. Pachifukwa ichi Mulungu sadatiyikeife kuti tilawe mkwiyo koma kuti tilandire chipulumutso mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.

10. Amene adafa m'malo mwathu, kuti, pamene tidzuka kapena kugona, tikhale ndi moyo pamodzi ndi Iye.

Nkhani ili pano ikuti, zilibe kanthu kuti tikufa Yesu asanabwere kapena tidzakhala ndi moyo pobwera Ambuye, komabetidzakhala pamodzi ndi Iye. Akhristu ena ambiri adatsogola kale pa njira ya imfa koma tonse tidzakhala pamodzi ndi Ambuye patsiku limenelo.Anzanga, tsiku limenelo tidzasonkhana pamodzi ndi Sitifano, Atumwi, ndi abale onse okhulupirira amene akugona mwa Ambuye.Tiyamika Ambuye chifukwa mwa chisomo chake tonse tidzasonkhana pamodzi ndi Iye.

Potsiriza Paulo akuti tiyenera kutonthozanandikumangirirana wina ndi mzake chifukwa cha chisomo chimenechi.

Tsopano Paulo akupereka malamulo kwaakhristu. Malamulowa alipo 22 osati khumi ayi. Mulungu akunena kuti inu, kufikira mutagonja ku mtandawaYesu, Mulungu akuna kuti mukhale womvera Mwana wake, amene adafera inu ndi ine pamtanda?'Koma mutalandira Yesu ngati Mbuye ndi Mpulumutsi, Mulungu akufuna kukonza moyo wanu. Ana a Mulungu amawonetsa chikondi chawo

kwa Mulungu posunga malamulo ake. Amawonetsa chikondi kwa Mulungu posunga malamulo a Mulungu ku ntchito, kusukulu, ku mudzi ,kulikonse komwe amapita.

Tamvani pa Yohane 14:15, Ambuye Yesu akunena kuti, "Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga."Paulo pavesi 8 adalamula kuti tibvale zobvala zotiyenera ngati ana a Mulungu, koma tsopano akutipatsa malamulo oyenera kutsata paulendo wathu wachikhristu.Malamulowaamagwira ntchito pamodzi mogwirizanam'magawoena a moyo wathu.

11. Mwa ichi tonthozanani, ndipo mangiliranani wina ndi mnzake, monganso mumachita

Lamulo loyambandilakuti "tonthozanani wina ndi mzake" kutanthauza kuti limbikitsanani wina ndi mzakem'chikhulupiriro.Lamulo lachiwiri ndilakuti 'mangiliranani wina ndi mzake'.Atesalonika amatsata malamulo awa koma Paulo akuwalimbikitsa kuti apitilize kukhala motero.Kukhala motonthozanandi kumamangilira wina ndi mzake.Kutanthauza kuti akhristu ayenera kukhala motonthozana ndi Mau a Mulungu kuti azikhalamomangirirana wina ndi mzake.

Lero tilekeza pano ndipo timasanthula1 Atesalonika 5:1-11, momwe takambirana kuti chiyembekezo chakudzakwa Kristu, chitifulumize kutumikira Mulungu.

Ambuye akudalitseni inu. Amen!